

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

PAMENE MVULA INABWERA

Inafika nthawi mu mbiri ya dziko pamene Mulungu anatsanulira chiweruzo chake ndi kuononga anthu chifukwa cha kuipitsitsa kwavo. Pamene mtundu wa anthu unali kuchuluka, "Ndipo anaona YEHOVA kuti kuipa kwa anthu kunali kwakukulu pa dziko lapansi, ndiponso kuti zonse za maganizo a mitima yao zinali zoipabe zokhazokha. Ndipo Yehova anamva chisoni chifukwa anapanga munthu padziko lapansi, ndipo anavutika m'mtima mwake. Ndipo anati Yehova, Ndidzafafaniza anthu amene ndawalenga padziko lapansi;" (Genesis 6:5-7).

Uchimowo unali waukulu kwambiri ndipo unachulukira chifukwa chakuti "ana aamuna a Mulungu" anayamba kukwatira "ana aakazi a anthu" (Genesis 6:1-2). Ana aamuna a Mulungu anali iwo amene anachokera ku mbadwo wa Seti ndipo anali ndi chiyambi cha kulemekeza ndi kuvomereza Mulungu wa Kumwamba. Iwo anayamba kukwatira ana aakazi a anthu amene anachokera ku mbadwo wa Kaini, anthu opembedza mafano komanso osapembedza. Zili zonna ndithu ngakhale m'dziko loipali kuti pamene anthu akwatira kunja kwa chikhulupiro, akukwatira kunja kwa chifuniro cha Mulungu; ndipo zotsatira zake ndi kugwa ku uzimu kwa iwo amene pa nthawi ina anali mu chiyanjano ndi Mulungu.

Mkati mwa kuipa kotere, "Nowa anapeza ufulu pamaso pa Yehova" (Genesis 6:8) chifukwa iye anali omvera ku chifuniro cha Mulungu. Mulungu anapereka njira yopulumukira kwa Nowa ndi banja lake ku chionongeko chimene chinali kubwera. Iye analangiza Nowa kuti amange chingalawa, popeza Mulungu anali kubweretsa chigumula cha madzi padziko lapansi chimene chidzaphe zamoyo zonse.

Nowa anali mlaliki wa chilungamo ndipo nzosakaikitsa kuti iye analengeza kwa onse

amene anamva za chionongeko ndi chiweruzo cha Mulungu chimene chinali kuyandikira. Chaka ndi chaka, anthu anatsutsana naye ndi kumunyoza, komabe Nowa anapitirira kugwira ntchito yomanga chingalawa molimbika ndi mwa chikhulupiro. Tsiku lina pamene Nowa anamaliza kumanga, ndipo nyama zonse zinalowa mu chingalawamo, Mulungu anauza Nowa kuti, "Talowani, iwe ndi akunyumba ako onse m'chingalawamo" (Genesis 7:1). "Pakuti akapita masiku asanu ndi awiri Ine ndidzavumbitsa mvula padziko lapansi" (4). Mulungu anawatsekera onse m'chingalawamo, ndipo pamene Nowa anali ndi zaka 600, akasupe a madzi a pansi pa dziko ndi madzi a m'mitambo anatsekulidwa. Kunayamba kugwa chimvula choopsa chimene sichinagwekonso padziko lapansi nkale lonse. Mulungu adachita zomwe adanena kuti adzachita, ndipo anthu onse adaonongedwa ndi chigumula kupatula okhawo omwe anali m'chingalawa. Iwo anaonongeka chifukwa anakana Mulungu Wamphamvuyonse.

Taganizirani mmene zinalili kwa anthu amene anaona munthuyu akumanga chingalawa. Iwo anamva chenjezo la chiweruzo chimene chinalikubwera, ndipo anauzidwa kuti atembenukire mitima yaho kwa Mulungu, komabe iwo ananyalanyaza uthengawo. Ndipo tsiku lina dontho la mvula linagwa kuchokera kumwamba. Posakhalitsa, kunagwa chimvula, ndipo wolambira mafano, wosakhulupiro. Mulungu komanso wokayikira zakuti kuli Mulungu onse anakhulupiro uthenga uja wa Nowa—koma nthawi inali itatha.

(Yapitirira pa tsamba 2)



**"Iwo anamva...
ndipo anauzidwa
kuti atembenukire
mitima yaho kwa
Mulungu, komabe
iwo ananyalanyaza
uthengawo.
Ndipo tsiku lina
dontho la mvula
linagwa kuchokera
kumwamba."**

ZIMENE BAIBULO

LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyerera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhaldwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Zikhoza kutheka kuti khamu la anthu linasonkhana kuzungulira chingalawacho pamene mvula imagwa ndipo amakuwa kuti, "Tilowetseni. Titsekulireni chitseko. Tipulumutseni!" Mwai wa chipulumutso ku imfa unali utapita, pakuti chitseko chinali chitatsekedwa. Nthawi inali itatha.

Monga mmene zinalili m'masiku a Nowa, zidzakhalanso choncho pamene Yesu adzabweranso padzikolo lapansi kuti adzatitenge kutifiksita kumpando wa chiweruzo wa Mulungu. "Ndipo monga masiku a Nowa, koteru kudzakhala kufika kwake kwa Mwana

wa Munthu. Pakuti monga m'masiku aja, chisanafike chigumula, anthu analinkudya ndi kumwa, analikukwatira ndi kukwatiwa, kufikira tsiku limene Nowa analowa m'chingalawa, ndipo iwo sanadziwe kanthu, kufikira kumene chigumula chinadza, chinapululutsa iwo onse, koteru kudzakhala kufika kwake kwa Mwana wa Munthu" (Mateyu 24:37-39).



"Wolambira mafano,
wosakhulupirira
Mulungu komanso
wokayikira zakuti
kuli Mulungu onse
anakhulupirira uthenga
uja wa Nowa—koma
nthawi inali itatha."

ndi Mulungu. Iyi ndi nthawi yokwera chingalawa cha chipulumutso. Tikukhala m'masiku otsiriza, ndipo nthawi ikutha. Yesu Khristu ali pakhomo ndipo dziko lino latsala pang'ono kuonongedwa ndi chiweruzo chomaliza cha Mulungu. Anthu akukhala ngati kuti dzikoli silidzatha. Dziko lapansi limanyoza woyerera wa Mulungu. Anthu amapeputsa chipunzitso cha chiyero ndi kuyeretsedwa. Anthu akungofuna njira zaozao ndi kutsatira zilakolako zao. Uchimo ndi zoipa zachuluka m'dzikolo lino. Posachedwapa zonse zidzatha. Mosakayika konse, Mulungu adzatumiza Mwana wake kudzaweruza monga mmene anatumizira chigumula padzikolo lapansi.

Tikukhala m'masiku otsiriza moto wa Mulungu usanatsanulidwe kuti uononge dziko lapansi komaliza. Yesu akadzabweranso, kudzakhala kochedwa kwambiri kuti alape. Ino ndiye nthawi yolapa. Kodi tichite chiyani kuti mukhulupirire? Nthawitu idzakhala itatha kwa inuyo. Nthawi ndiye ikutha. ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwalere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalamu zimene ena amapereka mwafulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA

editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Taonani, adza ndi mitambo; ndipo diso lililonse lidzampenya Iye, iwonso amene anampyoza; ndipo mafuko onse a padziko adzamlira Iye. Terotu. Amen. — Chivumbulutso 1:7

Tsiku lina, posachedwapa, Ambuye Yesu adzabwera ndi angelo ake kuchokera m'mitambo. M'kamphindi, m'kuphethira kwa diso, pa lipenga lotsiriza, ndipo nthawi sidzakhalaponso. Padzakhala kuonongeka kwa nyengo pamene nthawi idzatha ndipo anthu onse a mibadwo yonse, amoyo ndi akufa omwe, adzasonkhana pamodzi. Padzakhala chiukitso cha chilengedwe chonse, ndipo anthu onse adzaimirira pamaso pa mpando wachifumu waukulu woyerwa wa chiweruzo. Buku la moyo lidzatsegulidwa, ndipo tonse tidzaweruzidwa. Olungama adzalandira moyo wosatha Kumwamba kuti akakhale ndi Yehova kwa tuyaya, ndipo osalungama adzaponyedwa m'nyanja yamoto kwa tuyaya.

Mtolo wanga mu kalatayi ndi wa ulaliki m'maonekedwe ake. Pali choonadi chimene Mzimu wa Mulungu akufuna kuti woyerwa ndi wochimwa achigwire: Nthawi ndiye ikutha.

Mzimu wa Mulungu wayendayenda pa ine kambirimbi mu miyezi ingapo yapitayi, ndipo ndikupemphera kuti Mzimu Woyerwa achitenso ndi mzimu wanu pamene mukuwerenga kalatayi. Izi si zongolemba chabe, koma ndi chipunxitso china, uthenga wina. Kulira kwa Ambuye kwa umulungu kutikumbutsa kuti nthawi padziko lapansi yachepta. Kubwera kwa Ambuye kwayandikira kwambiri. Yesu akubweranso, ndipo ndi posachedwapa.

Tchimo ndi moyo wokonda zoipa pa dziko lino zili pamaso pa Yehova nthawi zonse. Monga mmene zinalili ndi Sodomu komanso Gomora, chiweruzo cha Mulungu chili pafupi kugwa. Thawitsani moyo wanu, ndipo mupulumutsidwe. Ngati munagwira ntchito koma simumakonda kapena kutumikira Mulungu ndi mtima wanu wonse, ino ndiyo nthawi yakuti musinthe. Dzichepetseni mtima wanu kwa Mulungu ndi kulirira kuti akuchitireni chifundo, popeza posachedwa, chifundo sichidzakhalaponso. Iwe amene wabwerera mmbuyo, lero ndi tsiku lobwereranso kwa Mulungu. Mudzakhala mukutalikana ndi Mulungu pokhapokha mutalengeza mwazi wa Yesu. Tiyeni tisabisale kuseli kwa dzina la banja lathu, mbiri ya mpingo, kudziwika lathu, kapena kutchuka kwathu mu mpingo. Tiyeni tichite momasuka ndi moona mtima pamaso pa Mulungu ndipo tiunguze miyoyo yathu ndi kutsimikizika kuti tikudziwa bwino zinthu zonse pamaso pa Mulungu wa Kumwamba.

Sitikudziwa tsiku la kubweranso kwa Ambuye ndipo kulira uku kwakhalapo kwa zaka zokwana 2000; komabe ifeyo tili pafupi kuposa ena onse akale, ndipo kulira kwa Mzimu kuti "Nthawi ndiye ikutha" ndi komveka komanso kodziwika bwino. Mverani chenjezolo. Musaganize kuti mawa lidzafika. Pali machimo ofunikira kulapa, zodetsedwa zomwe ziyenera zitsukidwe, maubale ofunikira kukonzedwa, ndi mitima yodzitukumula yomwe ikuyenera kuti idzichepetse. Ngakhale kuti ineyo pandekha sindikufuna kukhala wongochenjeza chabe, ndikutanthauza kuti ndikupereka chenjezoli mwa mphamvu ya Mulungu.

Tiyeni tikonze nyumba yathu, chifukwa nthawi yatsala pang'ono kutha. Tsiku lililonse tidziliona ngati kuti ndi lomaliza, chifukwa posachedwa tsiku lina lidzakhaladi lomaliza.

Michael W. Smith

October 2022



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapananso kuti

muone makalata akale.

NDIKUYENERA KUFA, KOMA LITILO?

**NDIKAKUMANA NDI MULUNGU.
KOMA MOTANI?**

NDIKAKHALA KWAMUYAYA, KOMA KUTIKO?



Kalozera powerenga Baibulo

Mutu: Chimaliziro chayandikira

Kuwerenga Malemba: Chifukwa chake khalani inunso okonzereratu; chifukwa munthawi m'mene simuganizira, Mwana wa Munthu adzadza. — Mateyu 24:44

Mwachidule: Malingana ndi malemba komanso mmene Mulungu amaonera nthawi ndiponso chiweruzo chake, nthawi padzikolo lapansi ikutha. Kubwera kwachiwiri kwa Khristu kuli pafupi. Konzekerani kukumana ndi Mulungu wanu.

I. Fanizo lofotokozena

Anamwali khumi (Mateyu 25:1-13)

II. Domgosolo ndi nthawi ya Chiweruzo cha Mulungu

- A. Adamu & Heva—Chigumula: ~ zaka 1656
- B. Kuchokera pa Chigumula—Chilamulo cha Mose: zaka zosaposera 900
- C. Kuchokera pa Chilamulo cha Mose—Imfa ya Khristu zaka zosaposera 1,500
- D. Kuchokera pa Imfa ya Khristu —Tsiku lalero: zaka zosaposera 2,000

III. Chiweruzo cha Mulungu

- A. Luka 17:26-29 Monga zinalili m'masiku a Nowa.
- B. Aroma 14:10-12 Onse adzaimirira pa chiweruzo.

IV. Nthawi idzatha mosayembekezera

- A. Chivumbulutso 16:15 Yesu adzabwera ngati mbala.
- B. 1 Atesalonika 5:1-3 Mtendere ndi bata; kenaka chionongeko modzidzimutsa.

V. Nthawi yoikika

- A. Mateyu 24:36 Atate yekha adziwa.
- B. Machitidwe 17:30-31 Iye wasankha tsiku limene adzaweruze dziko lapansi.

- C. Ahebri 9:27 Imfa ndi chiweruzo zili zoikika ndithu.
- D. Luka 12:16-21 "Usiku omwe uno moyo wako udzafunika."

VI. Chimaliziro chayandikira

- A. Aroma 13:11 "Chipulumutso chathu chili pafupi tsopano kusiyana ndi pamene tinakhulupirira."
- B. 1 Petro 4:7 Chitsiriziro cha zinthu zonse chili pafupi.
- C. Chivumbulutso 22:20 "Ndithudi ndidza msanga. Amen."

VII. Zinthu zomaliza

- A. 2 Petro 3:3-9 Onyoza komanso kuleza mtima kwa Mulungu.
- B. 2 Petro 3:10-12 Kodi mukhale munthu wamtundu wanji?

Kumaliza

Konza nyumba yako, pakuti iwe udzafa, sudzakhala ndi moyo. — Yesaya 38:1

Dongosolo ndi machitidwe a chiweruzo cha Mulungu malingana ndi nthawi



NTHAWI NDIYE IKUTHA



Dzuwa limatuluka ndi kulowa. Mivi ya pa wotchi imapitirirabe kuyenda. Anthu akukhala m'moyo ngati kuti mawa lidzakhalapobe mpaka kale, ndiponso ngati kuti adzakhala ndi mwai wina. Komabe, taima m'mbali mwa moyo wamuyaya, ndipo nthawi yatsala pang'ono kutha.

Khristu adzabweranso

Yesu akubwera posachedwapa ndipo akadzabweranso, dziko lapansi lidzaonongedwa. Tonse tidzaweruzidwa pamaso pa Mulungu ndipo kenaka tidzakhala ndi moyo kwamuyaya Kumwamba kapena ku Gehena. Sipadzakhalanso kuyeza kwa nthawi, chifukwa nthawi sidzakhalaponso. Kodi mwakonzeka?

Anamwali Khumi

Yesu ananena fanizo la anamwali khumi pa Mateyu 25:1-13 pofuna kutichenjeza za kubweranso kwake. Anamwali asanu anali ochenjera ndipo asanu anali opusa. Onse anali ooneka mwachipembedzo pamene anali kuyembekezera kuti mkwati afike. Asanu mwa anamwali amenewa, anthu amene anadzilekanitsa ku chisalungamo cha dziko, anachita mosasamala. Iwo analolera kusiya nyali yayo zoyaka mpaka mafuta onse anatha ndipo zinazima. Iwo anakhala ofunda ndipo chikondi chao pa Mulungu chinazilala. Chisomo cha tsiku ndi tsiku ndi mphamvu ya Mzimu Woyerza zinalibenso ufulu. Nthawi ina moto unkayaka, koma pa kupita kwa nthawi chifukwa cha kunyalanyaza moto unazima. Zoterezi ndi zimene akuchita anthu ambiri odzitcha Akhristu masiku ano.

"Ndipo pamene mkwati anachedwa, onsewo anaodzera, nagona tulo" (5). Mkwati akuchedwa kubwera kwake. Izi zikusonyeza kuti Khristu akuchedwa kubweranso kwake padzikola lapansi pano ndipo m'maganizo mwa anthu kuti "nthawi yadutsa kale." Pamene Iye anachedwa, anamwali onse anaodzera nagona, popeza panali pafupi

ndi pakati pa usiku. Inali nthawi ya mdima wa ndiweyani kupatula pamene pamayaka nyali zisani paja. Inali nthawi ya tulo komanso kusinza. Mfundu ya fanizoli si yakuti Akhristu onse adzakhala akugona, popeza pakhoza kukhala ena amene akudikirira ndi kuyembekezera kubweranso kwa Ambuye; koma pali chenjezo lakuti tikhale maso ndi kukhala tcheru komanso wokonzekera kubweranso kwa Yesu Khristu

"Koma pakati pa usiku panali kufuula, Onani, mkwati! Tulukani kukakomana naye" (6). Tili pafupi ndi pakati pa usiku. Dziko lapansi laphimbidwa ndi mdima wa uchimo ndi chinyeng pamene Mulungu akukankhidwira kunja kwa miyoyo ya anthu. Ndi pafupifupi pakati pausiku. Anthu ambiri akutsatira njira zao zodzikonda m'malo motsata ndi mtima wao wonse chiyero ndi umulungu wa Khristu. Khalani okonzeka mumdima uno kuti mukhoza kumva kulira kwa lipenga kuti Khristu wabweranso. Dziko lapansi likunka lizimirira mwansanga kuzinthu zauzimu, ndipo nthawi yatsala pang'ono kukwana 12 koloko ndipo zikatero nthawi ikhala kuti yatha.

Pamene mkwati anabwerera, anamwali opusa aja anapempha anza aja kuti awagawireko mafuta ao, koma tsoka ilo, naonso anatsala ndi ochepta. Monga lilili fanizoli, aliyense wa ife ali ndi udindo woyang'anira moyo wake wauzimu ndi zochitika zathu zauzimu pamaso pa Mulungu. Tiyenera kufunafuna Mulungu tsiku ndi tsiku ndikukhala okonzeka kubweranso kwa Ambuye. Fanizoli likutiphunzitsa kuti anamwali opusa anapita kukagula mafuta, koma atabwerera "ndipo anatseka pakhomu" (10). Iwo anali attachedwa monga momwe zidzakhalire Yesu akadzabweranso. Sipadzakhalanso mwayi wokonza zinthu zofunikira kwambiri, sipadzakhalanso nthawi yopemphepa ndi kupempha chikhululukiro, sipadzakhalanso nthawi yokonza zolakwika, sipadzakhalanso nthawi yosintha. Tonse tidzayang'anizana ndi Ambuye monga mmene tilili panthawiyo. Anamwali asanu opusawo anafuula kuti Ambuye atsegule chitseko, monga mmene anachitira m'masiku a Nowa kale lija pamene mvula inagwa.

(Yapitirira pa tsamba 6)

Ambuye anati, "Indetu ndinena kwa inu, sindikudziwani. Chifukwa chake dikirani, pakuti simudziwa tsiku lake, kapena nthawi yake." (12-13) Chotero dikirani!

Dongosolo la chiweruzo

Palibe chitsimikizo chakuti chaka chamawa tifika, ndipo palibe chitsimikizo chakuti mawa likhalapo. Munthu akaganizira za dongosolo ndi nthawi ya ziweruzo za Mulungu, n'zoonekeratu kuti nthawi ikutha. Adamu ndi Heva atachimwa, panapita zaka 1,656 kuti Mulungu atsanulire chiweruzo chake ndi kuononga dziko lapansi ndi chigumula. Kuchokera pa chigumula, panadutsa zaka zosaposera 900 kufika pa nthawi imene Mulungu anapereka chilamulo kwa Mose. Ndipo chilamulo chinakhala chikugwira ntchito kwa zaka pafupifupi 1,500 kenaka kunabwera nyengo ya Chisomo kudzera mwa Yesu Khristu. Ndipo tsopano padutsa zaka pafupifupi 2,000 kuchokera pa nthawi imene Khristu anatifera pamtanda kuti aombole mtundu wa anthu ku uchimo.



Tidikire mpakana liti?

Dziko lonse lathu lapansili lakana Khristu, ndipo uchimo wachuluka. Kodi Mulungu adzadikira mpaka liti asananene kuti, "Kwakwanira"? "Ndipo monga kunakhala masiku a Nowa, momwemo kudzakhalango masiku a Mwana wa Munthu" (Luka 17:26). Anthu adzakhala akudy, kumwa, kukwatira, kugwira ntchito, ndi kungokhala ndi moyo. Kenako, chiweruzo cha Mulungu chidzatsanulidwa. Ambuye akadzabweranso, "mabondo onse adzagwadira Ine [Khristu] ndipo maliliime onse adzavomereza Mulungu" (Aroma 14:11). Posachedwapa, sipadzapezeka osakhulupirira, chifukwa tonse tidzaona Khristu mu ulemerero

ndi ulamuliro wake wonse. Aliyense adzaimirira moyang'anizana ndi mpando wakuweruzira wa Mulungu ndipo akadzinenera yekha kwa Mulungu zimene anachita,

Chimaliziro chadzidzidzi

Nthawi idzatha mosayembekezereka, chifukwa Khristu adzabwera mwadzidzidzi. "Taonani, ndidza ngati mbala. Wodala iye amene adikira, nasunga zovala zake" (Chivumbulutso 16:15). Kodi mukusunga zovala zanu kuti zikhale zoyerwa ndi zosada, kapena mwadetsedwa ndi madonthomadontho a uchimo ndiponso ntchito za kuthupi? "Koma za nthawizo ndi nyengozo, abale, sikufunika kuti tidzakulemberani. Pakuti inu nokha mudziwa bwino kuti tsiku la Ambuye lidzadza monga mbala usiku. Pamene angonena, Mtendere ndi mosatekeseka, pamenecho chionongeko

chobukapo chidzawagwera" (1 Atesalonika 5:1-3). Sipadzakhalango chenjezo lina pamene Khristu adzabweranso kuposa izi zimene mukuwerenga tsopano. Zidzakhala zadzidzidzi komanso zosayembekezereka.

Palibe munthu amene akudziwa za tsiku ndi nthawi ya kutha kwa dziko kupatula Mulungu Mwiniwake. Yesu sadziwa nkomwe, koma "koma Atate yekha" (Mateyu 24:36). Atumiki ndi mabungwe achipembedzo anenera za nthawi yeniyeni ya kubweranso kwa Ambuye. Zimenezi zinali zopanda pake monga mwa thupi, pakuti malemba amaphunzitsa momveka bwino kuti Mulungu yekha ndi amene akudziwa. Komabe, Mulungu watipatsa ife Mau ake amene amatidziwitsa kuti tili m'masiku otsiriza komanso kuti chimaliziro chili pafupi.

Tsiku loikika

Mulungu "anapangiratu tsiku limene adzaweruza dziko lokhalamo anthu m'chilungamo" (Machitidwe 17:31). Iye ali ndi nthawi yoikika ndipo mwa zizindikiro zonse, tsikulo lili kuyandikira mofulumira. Palibe amene adzathawe nthawi yoikikayi. Pa Luka 12:16-21, Yesu ananena fanizo la munthu wolemera amene anali ndi malingaliro aakulu okhudza tsogolo lake. Iye anaganiza zogwetsa nkhokwe zake ndi kumanganso zina zazikulu ndi kukhala moyo wofewa ndi kusangalala nawo moyo wake. Mulungu anamuuzu kuti: "Wopusa iwe, usiku womwe uno udzafunidwa moyo wako" (20). Munthuyo anapita ku moyo wamuyaya ali wosakonzekera kukakumana ndi Mulungu. Ngakhale Ambuye satibwerera ife usiku uno, inoyo ikhoza kukhala nthawi yanu. Kodi mukukhala m'moyo wokonze ka pozindikira kuti moyo wanu ukhoza kufunidwa kwa inu? Simudzatha kusintha nthawi yoikiyayi.

Zoonadi, ndidza msanga

Nthawi ndiye ikutha. "Koma chitsiriziro cha zinthu zonse chili pafupi; chifukwa chake khalani anzeru, ndipo dikirani m'mapemphero" (1 Petro 4:7). Khristu anachitira umboni za izi kwa Yohane zaka zoposa 2000 zapitazo pamene anati, "Indetu; ndidza msanga" (Chivumbulutso 22:20). Kodi ali kuti panopa? Ndithudi, Iye akudikira ali pakhomu.

"Masiku otsiriza adzafika onyoza...ndi kunena, 'Lili kuti lonjezano la kudza kwake?'" (2 Petro 3:3-4). Zoonadi. Nthawi yatalika, koma Petro anawachenjeza iwo kuti monga momwe dzikoli linaonongedwera ndi madzi, lidzaonongedwano ndi moto. Mulungu ali wolezamtima ndiponso "wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa" (9).

Khalani okonzeka pamene iye akubwera

"Popeza izi zonse zidzakananganuka kotero, muyenera inu kukhala anthu otani nanga, m'mayendedwe opatulika ndi m'chipembedzo?" (2 Petro 3:11). Nthawi ndiye yatsala pang'ono kutha, ndipo Khristu abwera tsiku lina lililonse. Koma kodi mwakonze? Apo ayi, inoyo ndiye nthawi yolapa ndi kupempha Yesu kuti alowe mumtimi mwanu. Ino ndiye nthawi yokonza moyo wanu poyembekezera moyo wosatha. Ngati simuli wokonze ka kugonja panopa, ndilibe chikaiko kuti inuyo mudzakhalango osakonzeka ngakhale mawa. ■

CHENJEZO LOONA

(Bible Lessons, Vol 17 No. 4, 1985)

Leslie C. Busbee



Kuchokera kwa Petro ndi Paulo, ndi Yakobo tili ndi mauneneri okhudza kubweranso kwa Yesu. Masiku akuthamanga pamene tikuyandikira ku tsiku lalikulu ndi lomaliza pamene zinthu izi zidzakwanirtsidwa....Tiyeni tikhale otsimikiza kuti Iye adzasungadi lonjezo lake ndipo adzabweranso monga momwe zinanenedweratu. Masikuwo ali pafupi kuposa momwe tikuganizira. "Pamene angonena, Mtendere ndi mosatekeseka; pamenepo chionongeko chobukapo chidzawagwera." Mmene dziko likuthamangira masiku ano, anthu akufuna mtendere ndi chitetezo. Sizitengera kuti munthu umayesetsa bwanji kuti ukhale woteteze ka mu dziko ili loipali, kapenanso amakhalira olemera pa zinthu zathupi zokhudza moyo uno; zonsezo zidzachotsedwa kwa iwo m'kamphindi. Khristu akadzabwera dzikoli lidzaonongedwa. Sipadzakhala china choikidwa pakati pa mkwatulo ndi masautso kuti chiwapatse anthu mwai wina wokonzekera kukumana naye. Yesu akadzabwera, akufa adzaukitsidwa, oyera ndi ochimwa, onse oipa ndi abwino, olungama ndi osalungama omwe. Zonse zidzachitika nthawi imodzi. Iye adzabwera kudzapereka chilango kwa iwo amene sadziwa Mulungu, ndi kulemekezedwa mwa oyera ake. Sipadzakhala kuima kwa zaka chikwi pakati pa kuukitsidwa kwa olungama ndi oipa. Koma ifeyo ngati tikhale okonzeka kuti tilandiridwe ndi Iye, tidzayenera kuhala mu chikhalidwe chimenecho pamene Iye adzabwera. Kudandaula konse, njiru, ndeu, kaduka ndi kuwawidwa mtima ziyanera kutuluka m'mitima yathu. Izzi zidzatanthauza chinthu chachikulu kwa ife kuti tidzawerengedwe kuhala oyenerera kuima pamaso pa Mwana wa munthu tsiku limenelo.

Kufuna kuhala wokonzekera kukumana ndi Ambuye ndiye chinthu chofunikira kwambiri komanso chikhumbo chapamwamba cha mwana wa Mulungu. Zimenezi ziyanera kuhala m'maganizo mwathu tsiku lililonse. Lero likhoza kuhala tsikulo. Mitima yathu ndi malingaliro athu akuyenera kuhala kutali ndi dziko loipali ndipo akhazikika pa chuma chomwe chili kumwamba kumene Khristu wakhala pa dzanja lamanja la Mulungu komwe akuyembekeza kufikira tsikulo pamene Iye adzabwerenso. "Khristunso ataperekedwa nsembe kamodzi kucasenza machimo a ambiri, adzaonekera pa nthawi yachiwiri, wopanda uchimo, kwa iwo amene amlindirira, kufikira chipulumutso" (Ahebri 9:28). Paulo ananena kuti korona wa moyo adzapatsidwa kwa onse "okonda maonekedwe ake."Ha!, ngati tikhala mokhulupirika kwa Iye ndi kumuika Iye pamwambamwamba mu mitima yathu ndi malingaliro athu, tidzamulandira Khristu waulemerero akubwera kuchokera m'mitambo ya kumwamba wokutidwa ndi mphamvu ndi ulemerero waukulu! Tikulimbikitsidwa kuhala anthu amene malankhulidwe athu onse akhale oyera ndi opembedza, ndipo tipezedwa mwa iye mu mtendere, opanda bangwa ndi opanda chilema. Awa ndi machenjezo oona ndipo ndi cholimbikitsa kwa ife. Yesu anatiuza pa Luka 21:36 kuti: "Koma inu dikirani nyengo zonse, ndi kupemphera, kuti mukalimbike kupulumuka zonse zimene zidzachitika, ndi kuimirira pamaso pa Mwana wa Munthu." Kodi sikungakhale kopindulitsa kuvutika monga Mkhristu ndi kukalandira mphotho kumeneko! Tangoganizani za oyera mtima amene anatisogolera akuukitsidwa ku moyo ndi mphamvu ndi kupatsidwanso moyo wina! Chaka chikubwerachi chikhoza kuhala chomaliza padzikolo lino lapansi. Ngati kubwera kwa Ambuye kuli kutali ndi zaka 20, ndiye kuti titha kunena kuti tayandikira kwambiri, si choncho nanga? Ngatinso kwatsala zaka 10 zokha kuchokera pano, ndiye kuti kuyandikira kwake ndi kwambiri zedi. Kapena ngati zili zaka zisanu, apo ndiye tayandikira zenizeni pamphuno mpakamwa! Pakuti izi ndi nthawi zazing'ono kwambiri, zomwe zidzadutse posachedwapa. Tilole Ambuye atsogolere mitima yathu mu chikondi chake ndi kuyembekezera Khristu moleza mtima. ■



"Lero likhoza
kuhala tsikulo.
Mitima yathu
ndi malingaliro
athu akuyenera
kuhala kutali ndi
dziko loipali ndi
kuhazikika pa
chuma chomwe
chili kumwamba."



KODI MUKUDZIWA?

"Kubweranso kwachiwiri kwa Khristu ndi mfundo imene imakambidwakambidwa mu Chipangano Chatsopano. Nkhaniyi imatchulidwa koposera ka 8 poyerekeza ndi nkhanzi ya kubwera koyamba kwa Ambuye. Iyoyi imatchulidwa koposa ka 300 mu Chipangano Chatsopano."

("Facts About the Second Coming of Christ." Christian Courier. 9/20/2022).



DIKIRANI MODEKHA KUBWERANSO KWA AMBUYE

Lezani mtima inunso, limbitsani mitima yanu; pakuti kudza kwake kwa Ambuye kuyandikira. — Yakobo 5:8

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Ngakhale kuti uchimo uli wochuluka m'dziko ndipo misozi ya moyo imatuluka, koma monga ana a Mulungu, tili ndi chiyembekezo chodabwitsa ndi chowala chakuti tsiku labwino likubwera. Kubwera kwa Ambuye si chinthu choyenera kuchiopa kwa iwo amene apulumutsidwa. Tikuyembekezera mwachidwi tsiku limene Ambuye Yesu adzabwera kuchokera m'mitambo ndi kutitsogolera ku malo athu amuyaya Kumwamba. Sikudzakhalanso misozi, kusweka mtima, kupweteka, matenda, kapena zolemtsa kwa okondedwa amene amene anatayika; popeza tonse tidzakhala pamaso pa lye amene anatikonda ife napereka moyo wake chifukwa cha chiombolo chathu. Nyimbo ija yakuti, Kuyembekezera Kowala, imanena kuti: "Ndikudikirira, ndilakalaka kuitanidwa, Ndikamasuka kuchisoni ndi m'masautso; Pamene ndili ndi Yesu ndidzalamulira m'nyumba ya kumwamba, Kumeneko ndidzaona kukongola kwake kosatha."



Ha! tsikulo lidzakhala lodabwitsa koposa Kumwambako; komabe, sitinafikeko. Pamene zolemtsa zachuluka ndipo usiku ukuoneka ulibe malekezero, gwiritsitsani mwachikhulupiriro, "pakuti kudza kwake kwa Ambuye kuyandikira." Anthu ena amakhazikika mumkhalidwe wachitayiko ndipo chiyembekezo chao cha Kumwamba chimachoka. Ena amagonjera ku ziphunzitso ndi zilakolako za dziko lino lochimwali ndipo amataya khama lawo ndi cholinga chawo pa Mulungu. Enanso amalola kuti chikondi chawo chizilale chifukwa cha zipsinjo ndi mdima wa moyo uno.

M'bale ndi mlongo, dikirani modekha ndipo mupumule podziwa kuti chiombolo ku chigwa chachisonichi chikubwera posachedwa. Tisatengeke ndi zochitika m'dziko, koma tiyeni tikhazikitse ndi kuika mitima yathu mu chikondi cha Khristu. Tiyeni tiponye maso athu pa Yesu—kudikira modekha, kukumba mozama mu chikondi cha Mulungu, kugwira ntchito chifukwa cha miyoyo, ndi kukhala maso ndi kusamalitsa pa moyo watsiku ndi tsiku. Tisaimike manja athu mmwamba chifukwa cha kukhala kakasi ndi kukhumudwitsidwa, koma tiyeni tidikire modekha—pakuti kubwera kwa Ambuye Yesu kwayandikira. ■